

Komiti Yofufuza za Umoyo wa Anthu mu Zimbabwe (ZimLAC)


Kafukufuku wa Umoyo mu Midzi wochitidwa mu 2024

Malemba ofotokoza zotuluka mu kafukufuku

Bungwe lofufuza za Umoyo wa Anthu mu Zimbabwe (ZimLAC) likupitilizabe kufufuza makhalidwe a anthu chaka ndi chaka pokwaniritsa zomwe zinalumbilidwa m'chigawo 6 cha Lamulo la Kupeza Chakudya Chokwana Chomanga Thupi M'dziko (Food and Nutrition Security Policy). Kafukufuku wa 2024 anachitidwa potengera kusagwa kwa mvula mu nyengo ya 2023/2024 kochitika chifukwa cha El Niño. Kufufuza uku kunatsogoleledwa ndi kufunikira kwachangu kwa Boma la Zimbabwe kuti lizindikire zomwe El Niño idadzetsa chilala m'mabanja akumidzi ndikupereka umboni wodziwitsa kupanga zisankho.


1. Kuchepa kwa Zomera za Phala

Kuchepa kwa zomera za phala kuli kuyembekezeka kukhala 57% munthawi yanjala yaikulu (kuchokela pa Januwari mpaka Marichi 2025) mchaka cha 2024/25.



Mulingo wa Kuchepa kwa Zomera za Phala: 2020 – 2024

Kuchepa kwa zomera za phala mu mabanja kunawonjezera mu zigawo potengera kusagwa bwino kwa mvula.





Kusowa Chitetezo kwa Phala

Kuchuluka kwa Anthu Ochedpedwa ndi Zomera za Phala pa Chigawo Chimodzi cha Zigawo Zinayi za Chaka Chonse.

Gawo	Julaye - Seputembala	Okotobala - Desembala	Januwale - Marichi
Manicaland	872,817	980,800	1,049,770
Mashonaland Central	589,623	664,423	728,640
Mashonaland East	751,828	854,404	914,643
Mashonaland West	596,581	697,741	787,053
Matabeleland North	346,258	393,879	427,389
Matabeleland South	250,472	291,199	327,386
Midlands	656,232	749,023	819,984
Masvingo	669,297	760,863	839,503
Dziko lonse	4,733,107	5,392,332	5,894,368


Zigawo zoyembekezedwa kukhala ndi anthu ochuluka omwe akuchepedwa ndi zomera za phala pofika mlingo wa njala yayikulu ndi miliyoni ndi mazana anayi a mphindi ndi mazana asanu ndi awiri omwe ali ndi khumi zisanu ndi ziwiri (1,049,770) a ku Manicaland komanso mphindi mazana asanu ndi anayi ndi khumi zinayi ndi mazana asanu ndi limodzi ndi khumi zinayi ndi zitatu (914,643) a ku Mashonaland East.

2. Kuweta Ziweto



3. Kulima Zomera

Chiwerengero cha mabanja omwe amalima zomera chinatsika pa zomera zonse, kupatula manyuchi omwe adakwera kuchoka pa zigawo khumi ndi zisanu ndi zinayi kuchokera muzana (19%) mu 2022/23 kufika pa zigawo khumi ziwiri ndi zitatu kuchokera muzana (23%) mu nyengo ya 2023/24.



Mabanja omwe amalima zomera

Nyengo yokolola


Gawo	Chimanga		Manyuchi		Mapira Oyera		Mapira Onenepa		Chiwerengero cha Phala	
	Zoyembe kezera (makg)	Zomwe zilipo (makg)	Zoyembe kezera (makg)	Zomwe zilipo (makg)	Zoyembe kezera (makg)	Zomwe zilipo (makg)	Zoyembe kezera (makg)	Zomwe zilipo (makg)	Zoyembe kezera (makg)	Zomwe zilipo (makg)
Manicaland	1152	105	53	6	6	1	26	3	1236	115
Mash Central	894	107	251	10	0	0	2	0	1147	117
Mash East	809	88	46	2	6	1	2	0	862	91
Mash West	1240	50	99	4	1	0	1	0	1341	54
Mat North	425	30	169	39	5	0	123	30	723	99
Mat South	394	26	109	19	3	0	37	8	542	53
Midlands	1093	136	153	9	6	0	4	0	1257	145
Masvingo	651	61	245	28	17	2	100	16	1013	108
Dziko lonse	837	77	140	14	5	1	35	7	1016	99

Mabanja ankayembekezera kukolola 837kgs za chimanga komanso manyuchi ofika 140 kgs koma anakolola chimanga cholema 77kgs komanso manyuchi olema 14kgs.

4. Ndalama yobwela m'banja


Njira Zopezera Ndalama

Poyerekeza ndi chaka choyambira (2020), ndalama za mabanja akumidzi zikuwonjezeka.



Mlingo Wopezera Ndalama: 2020-2024

Malipiro a pa Mwezi a Banja (USD) a Epulo 2024




Malipiro a pa Mwezi a Banja

Malipiro a pa mwezi a banja anatsika kuchokera pa USD 116 mu 2022 kufika pa USD 88 mu 2024.

Kochokera Ndalama


Mabanja ambiri amadalira ntchito wamba amafika makhumi anayi kuchokera muzana (40%), ulimi wolima chakudya amafika khumi ndi zisanu ndi limodzi kuchokera muzana (16%) ndi ndalama zochokera mu Zimbabwe zofika makhumi awiri ndi limodzi kuchokera muzana (21%).



Kochokera Ndalama za Mabanja Kofunikila

5. Thandizo la Umoyo


Mabanja ambiri (43%) akuti adalandira thandizo kuchokera ku Boma motsatiridwa ndi UN/NGOs (6%) ndi achibale akumatawuni (5%).



Kochokera Thandizo

6. Madzi, Ukhondo ndi Kuwoneka Bwino (WASH)

Chiwerengero cha mabanja omwe ali ndi madzi mu mldzi chinatsika kuchoka pa 21% mu 2023 kufika pa 6% mu 2024.




Mtunda Woyenda Kukafika Komwe Kupezeka Madzi

7. Thanzi la Mwana

Kuwonjezedwa kwa Vitamini A


Chigawo cha chikulu cha Matabeleland North chofika (99%) chili ndi ana a miyezi (6-11) amene analandira mlingo wofunikira wa Vitamini A.



Kuwonjezedwa kwa Vitamini A

8. Machitidwe a Kupatsa Chakudya kwa Khanda ndi Mwana Wamng'ono

Kupatsidwa Chakudya Chofunikila kwa Khanda ndi Mwana Wamng'ono




Kupatsidwa Chakudya Chofunikila kwa Khanda ndi Mwana Wamng'ono

- Ana ofika 2.3% adapeza chakudya chovomerezeka chochepa, kuchepa kuchokera pa 4% mu 2023. Izi zikukhalabe pansi pa cholinga cha dziko cha 25%.
- Kusiyanasiyana kwa zakudya kunalinso kotsika pomwe 4.8% yokha ya ana amadya zakudya zosiyanasiyana.

9. Mayimidwe a Chakudya Chomanga Thupi la Mwana

Kupeza Chakudya Chomanga Thupi kwa Ana a Miyezi 6-59

Gulu lokhudza za thanzi la anthu padziko lonse la World Health Organisation linati chiwerengero cha ana omwe sakula bwino kudzera ndi kusoweka kwa chakudya chokwana kukhadali pa mlingo wa pamwamba chifukwa ukadali pa (27.4%).



Kupeza Chakudya Chomanga Thupi cha Ana a Miyezi 6-59

10. Mapeto ndi Malangizo

Boma ndi maBungwe omwe lili nawo pa Chitukuko akulangizidwa kuti apitirize kugwilitsa ntchito malangizo muzotsatira:

- a) **Kupezeka kwa Chakudya Chokwana:** Mabanja oposa 20 pa 100 aliwonse omwe analibe phala wokwanira kuti amalize chaka chathachi asonyeza kuti adzagwiritsa ntchito ndalama zosungira, zopezera komanso zogulira phala kumsika. M'pofunika kuti Unduna woona za Ulimi ndi maKampani oziyimirira aziona kuti mbewu za phala zizipezeka pamsika wa mabanja omwe ali ndi vuto la phala ndi njira zogulira kuti zitheke m'chaka chonsecho. Lingaliro ili lakhazikidwa pa Boma kusunga dongosolo la ufulu wa malonda a zomera.
- b) **Chitetezo mu Makholidwe:** Thandizo la anthu latsika kuchoka pa 74% kufika pa 48% chifukwa cha kuchepa kwa chakudya chomwe chinalipo mchaka chathachi. Kafukufuku wa Umoyo wa ku Midzi waZimLAC womwe unachitidwa mu chaka cha 2024 wapereka umboni wokwanira woti pakufunika kulimbikitsa madera omwe ali pachiwopsezo, makamaka poyang'anizana ndi chilala chomwe chinayambitsa El Nino komanso zododometsa ndi zovuta za mtsogolo. Thandizo liyenera kuganizira za kusatetezeka kwa magulu a anthu. Mabanja omwe ali ndi antchito akulimbikitsidwa kuti azichita nawo ntchito zaboma komanso pulogalamu ya zakudya kuti athe kulimba mtima kuti apewe kudalira kwa opereka thandizo.
- c) **Malipiro a banja:** Mabanja ambiri akumidzi amadalira njira za ulimi zomwe zingatengere kusintha kwa nyengo kwa nthawi yayitali. Ndalama zomwe anthu amapeza pamwezi zidatsika kuchoka pa USD 116 mu 2023 kufika pa USD 88 mu 2024, zomwe zikuwonetsa momwe umoyo wakumidzi udakhudzidwira chifukwa cha kusayenda bwino kwanyengoyi. Pakufunika kupitiriza kupititsa patsogolo njira za umoyo wakumidzi zomwe zikulimbana ndi zovuta za ulimi.



FNC ipezeka pa SIRDC: 1574 Alpes Road, Hatcliffe, Harare

Lamya: +263-242-862586/ +263-242-862025. Webusayite: www.fnc.org.zw. Imeli: info@fnc.org.zw.

Tiwita: @FNC_Zim. Inisitagiramu: [fnc_zim](https://www.facebook.com/fnc_zim). Fesibuku: Food and Nutrition Council Zimbabwe. Yuchubu: FNC Zimbabwe. Watsiapu: +263 0776 990 479